# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO**


**ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA MACHINGA M'DZINJA LA 2024-2025**

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya mvula ya 2024-2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira koposa mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.

Boma la Machinga likuyembekezeka kudzalandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kupyolera m'dzinjali komabe pali kuthekera kwa ng'amba yopafupifupi masiku khumi mmwezi wa February 2025.


## October 2024




Nyengo yotentha ikuyembekezeka m`mweziwu. Komabe mvula ya Chizimalupsya ikhoza kudzagwa pa mlingo wa ochepera 20 mm omwe ndi mlingo wokhazikika kapena kuposera m`madera ena a Machinga m'mweziwu.

Mvulayi ikhoza kudzagwa ndi mphepo ya mkuntho komanso ziphaliwari.

## November 2024





Boma la Machinga likuyembekezereka mvula yocheperako pofanizira ndi dzinja lapitali mu mwezi wa November. Mvula ya mlingo wa 25 mpaka 50mm omwe ndi mlingo okhazikika komanso kuchepera ikhoza kuzagwa m`madera ena.

M`madera monga a TA Nyambi akhoza kuzalandira mvula yocheperako.

Mvulayi ikhoza kudzagwa ndi mphepo ya mkuntho komanso mabingu.


## December 2024




Mvula yochuluka ikhoza kudzagwa ndi mlingo wa 150 mpaka 250 mm womwe ndi mlingo wokhazikika komanso kuposera m'mweziwu. Mvula yambiri idzagwa m`madera a TA Liwonde ndi kummawa kwa Machinga boma, komabe yocheperako ikuyembekezeka kwa TA Nyambi.

Mvula yodzalira ikhoza kudzayamba m'sabata loyamba la mwezi wa December


## January 2025




Mvula ya mlingo wa 250 mpaka 360mm ikuyembekezeka mu January. uwu ndi mlingo okhazikika komanso kupyolera. Motero mvulayi izaposera ya dzinja lapitali. Madera a pakati pa TA Liwonde ndi SC Chikwewo komanso liwonde town akhoza kuzalandira yochulukirapo.

Tiyembekezere Ng`amba ya sabata limodzi m`madera ena.


## February 2025




Madera ambiri akhoza kuzalandira mvula ya Mlingo wokhazikika kapena kuposera. Mlingowu ndi wa pakati pa 140 mpaka 280mm womwe ndiwoposanso dzinja la chaka chatha. Madera akum'mawa kwa Machinga monga kwa SC Ngokwe mvula idzacheperako.

Ng'amba ya sabata ziwiri komanso mphenzi zikuyembekezeka.


## March 2025




Mwezi wa March madera ambiri akhoza kudzalandira mvula ya mlingo woypolera okhazikika. Mvulayi ikuyembekezereka pa mlingo wa 130 mpaka 220 mm. Iyinso ndi mvula yochuluka m`mweziwu kuposera chaka chatha.

Mvula ikhoza kuzayamba kupita kumapeto m`sabata yomaliza ya March.

## April 2025




Nyengo ya dzinja ikhoza kudzatha kumayambiliro kwa mwezi April.

Mvula ya mlingo wokhazikika komanso oposera wokhazikika ikuyembekezeka ndi mlingo wa 20 mpaka 50mm, koma madera akwa TA Nyambi ndi SC Ngokwe ikhoza kudzafika 60 mm.


Mvula ya mlingo wokhazikika komanso kupyolera ikuyembekezeka ku machinga mu dzinjali kupatulapo mwezi wa November omwe ikhoza kuzachepera mlingo wokhazikika

Mvula yodzalira ikhoza kudzayamba m'sabata loyamba la mwezi wa December 2024 ndi Mathero a dzinja akuyembekezeka kuyambira m'sabata lotsiriza la March 2025. Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kudzakhala yayitali masiku apakati pa 80 mpaka 120.

Ng'amba yotalika sabata limodzi ikuyembekezeka m'mwezi wa January ndinso pafupifupi masabata awiri mu February 2025.

**NTAJA**

| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
|---|---|---|---|
| OCT | 0.3 | 9.4 | 17.5 |
| NOV | 32.3 | 78.8 | 35.3 |
| DEC | 150.9 | 232.5 | 189.7 |
| JAN | 215.8 | 304.0 | 353.4 |
| FEB | 134.5 | 222.2 | 225.2 |
| MAR | 87.0 | 179.6 | 154.8 |
| APR | 22.1 | 47.7 | 27.3 |





**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**

The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.

Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: